# EXAMINATIONS COUNCIL OF ZAMBIA

**Examination for General Certificate of Education Ordinary Level**

## Cinyanja 3156/2

**Pepala la Ciwiri**

**Wednesday** **9 AUGUST 2017**

Zina Zofunikira
Buku la mayankho

**Nthawi: Maola Awiri**

**Malangizo Kwa Olemba Mayeso**

Lemba dzina lako, nambala yamalo komwe ulembera mayeso ndiponso nambala yako iwe amene ulemba mayeso. Ulembe izi m'malo omwe apatsidwa mukabuku kamayankho.

www.eczpastpapers.com

Pepala la mayeso iri liri ndi zigawo zinai **A**, **B**, **C** ndi **D**.

Mukakamizidwa kuyankha mafunso onse opezeka pa cigawo ciriconse ca pepala lino.

Lemba mayankho ako m'kabuku ka mayankho komwe kapatsidwa.

Ngati wagwiritsira nchito mopitirira kabuku kamodzi, umange pamodzi mwatsatane-tsatane timabuku tonse timene wagwiritsa nchito.

Uziwerenga mobwereza-bwereza ndi kumvetsetsa malangizo omwe alembedwa pamwamba pafunso liri lonse.

**Zina Zolangiza Olemba**

Nambala ya mamaliki yaikidwa mu mfungako [ ], kumatsiriziro a funso lirilonse kumbali la funso kapena kumphepete kwa funso, mwatsatane-tsane.

**Malamya ya m'manja siyaloledwa m'cipinda colembera mayeso.**



www.eczpastpapers.com

## A CIGAWO COYAMBA – KUMASULIRA [MAMALIKI 20]

**Mukakamizidwa kuyankha funso lotsatirali m'Cinyanja comveka bwino ndiponso coyenera. Tsopano tembenuzani nkhani imene iri m'munsimu.**

**Determination pays**

The happiest moments of our lives come when we accomplish something that we never expected. The unexpected, however, to be appreciated, should be the resultant of our personal efforts. I remember when I was still in Grade 10 how I used to fail in all the subjects. In Grade 11, my performance became even worse such that there was no single subject that I got above 50%. I was never free to mingle with my peers especially when they would bring in school related stories.

It was during the December holiday that I sat down and reflected on my previous performance. I thought about how my parents suffered and sacrificed a lot just to see me forge ahead with my school. This was my turning point. I could not wait for schools to re-open so that I could put to effect the study techniques I had set during the holidays. My final year surprised many. Both teachers and my fellow learners were very amazed at my performance. Here I am studying medicine at University of Zambia (UNZA).

www.eczpastpapers.com

## B CIGAWO CACIWIRI - CIFUPIKITSO. [ MAMALIKI 20]

**Werengani mosamala nkhani yotsatira iyi, ndipo pambuyo pake mulembe nsatso yokoka mitima anthu.**

Yerekezani kuti ndinu Kalembera wa Kagulu ka acinyamata komwe kasunga nkhuku za mazira ndi ng'ombe za mkaka. Colinga ca kaguluka ndi kugulitsa mazira ndi mkaka.

Dzina la malonda la kagulu aka ndi 'Kadzipalire' komwe kapezeka m'boma la Kapangulula munsi mweni-mweni mwa mtsinje wa Mzime kumanzere kwa cipatala ca Kapangulula. Nambala ya lamya ya malonda ndi 0977444444.

Pofuna kukuthandizani kutstatsa malonda anuwa, pepala la nkhani (news paper) lakupemphani kuti mulembe nsatso (advert).

Lembani nsatso yokoka mitima anthu kuti atunthike kudzagula mazira ndi mkaka kucokera ku kabungwe kanuko.



www.eczpastpapers.com

## C CIGAWO CACITATU – MVETSO [MAMALIKI 30]

**Werengani nkhani iri munsimu ndipo bwino lake muyankhe mafunso otsatira.**

### Kudzikonda

Kudzikonda ndi khalidwe loipa lomwe munthu akhala nalo, likangamira mwa iye, sapenya anzake ngati anthu ai. Amadziyesa kuti iye ngopatulika ndiponso wosafanana ndi anzake. Popatsidwa zinthu, amakhumba kulandira gawo lalikulu kuposa anzake. Ndipo nayenso pogawa zinthu, amakonda kupatsa mnansi wake zambiri, anthudera amawapatsa kwayawausiku.

Pa mudzi wina wochedwa Mphatso, panali mkazi dzina lake Mwananiwako, amene anali ndi mwana wamwamuna m'modzi, koma wanthengo. Ndipo pocita mphumi, anakwatiwa ndi mwamuna wina wokoma mtima ndi wofatsa ngati nkhosa. Munthuyo anakwatira kale koma mkazi wake anagonera dzanja ndi kumusiira tiana tiwiri tatimuna tokha. Atapeza **nkhali** ina pamudzi wa Mphatso, anatenga anawo cifukwa cinali cola cake. M'masiku woyamba a ukwati wao, a bambo Mvetsa anamlangiratu mkazi wao uja, Mwananiwako, kuti atsate maleredwe abwino cifukwa ana aja anali ao onse. Ndipo zonse zinayenda bwino m'masiku woyamba aja.

www.eczpastpapers.com

Patatha miyezi yambiri, mkazi uja anaona kuti mwana wake ankaoneka ndi thupi lozimbwa-zimbwa, pamene ana awiri a mwamuna wake anali ndi matupi wopantha bwino. Sanafune kufufuza zifukwa zowondera mwana wake kweni-kweni, koma maganizo ake anathamanga kwambiri motero kuti anatsimikiza ndi mtima wonse kuti ali kumudya thupi ndi anzake aja. Ankaganiza kuti ali kumuondetsa cifukwa pakudya amamuzyerera. Anzake aja amadya pakulu ndipo mwana wake amadya **motongodzola**. Sanakhulupirire kuti anail kuonda ndi matenda ena. Tsono mosafunsa kwa wina aliyense, Mwananiwako, anasintha khalidwe loyamba lija. Amati akapita ku msika kukagula zakudya monga mondokwa, mbatata, malalanje ndi zina, anali kugula mondokwa uwiri, mbatata ziwiri ndi malalanje awiri. Sankafuna kugula zokwanira kuti mwana aliyense alandire mofanana ai. Kunyumba amacita mocenjera kuti ana a mwamuna wake aziti akonda iwo kwambiri. Ndipo popeza analidi ana ndithu, sankazindikira kanthu kuti mai uja anali **ndipsi**. Pogawa, amatenga mondokwa uwiri napatsa ana a mwamuna wake. Kenaka, amawauza kuti aliyense athyole pakati ndi kupatsako mwana wake.



www.eczpastpapers.com

Ana aja ankakondwera kuti mai anali kuwakonda cifukwa cakuti iwo ndiwo amagawirako mnzawoyo. **Ucitsizi** wa mkazi uja sunali kuoneka cifukwa akamapatsa mwana wake mondokwa uwiri wothyola, nkakhala mtsononkho wathunthu. Mwana wake ndiye anali kudya cimanga **camomwe**. Ndipo magawidwe anali wotero ngakhale ku nthoci, mbatata ndi malalanje. Mwana wake ndiye amadya pakulu.

Koma ukacenjede wake sunapite patali. Tsiku lina a Bambo Mvetsa anadabwa pakuona tizitsononkho tinai tothyola m'nyumba mwao. Pofunsa kwa ana, anaulula zonze za m'mene mai amagawira zinthu. Anauluładi cifukwa analibe mbiso, ndiponso ana alibe coka n'nene ai. Pomufunsa Mwananiwako, anakolokota pansi, nagwira mwendo wa mwamuna wake.

**Mafunso:**

**Tsopano yankhani mafunso wotsatira awa.**

**1** Kodi mai ali m'nkhaniyi mungamzindikire bwanji kuti ndi wodzikonda? ... [2]

- **A** Anali kudya zambiri iye yekha.
- **B** Pogawa zinthu amapatsa mwana wake zambiri.
- **C** Anali kukhala pa nyumba yekha.
- **D** Anali kufuna kulandira gawo lalikulu yekha.www.eczpastpapers.com

**2** Ndani anakwatira pamudzi wa mphatso? [2]

- **A** Bambo Mwananiwako
- **B** Bambo wa mkulu
- **C** Bambo Mvetsa
- **D** Bambo ucitsizi

**3** Kodi Mwananiwako anacembeza kangati? [2]

- **A** Kawiri
- **B** Kamodzi
- **C** Katatu
- **D** Kambiri

**4** Mbanjali munali ana ... [2]

- **A** atatu.
- **B** anai.
- **C** asanu.
- **D** ambiri.



www.eczpastpapers.com

5 Kodi mkazi wa m'nkhaniyi, anali kugawa bwanji zakuday? [2]

A Ziwiri-ziwiri mwana aliyense.

B Zambiri mwana wake.

C Zambiri ana a mwamuna wake.

D Zambiri mwana aliyense.

6 Tikati mwana wamthengo ndiko kuti mwana ... [2]

A woyenda –yenda mthengo.

B wobadwira mthengo.

C yemwe makolo anakumana kuthengo.

D wobadwa popanda cikwati ca makolo.

7 Kodi kudya kotongodzola ndi kudya kotani? Kudya ... [2]

A pang'ono-pang'ono.

B mofulumira.

C monyemerana.

D mosayembekezerana.

8 Mau akuti 'kugwira mwendo'atanthauza ciani? [2]

www.eczpastpapers.com

A Kugwiradi mwendo.

B Kugwada popempela.

C Kupepesa kwakukulu.

D Kulemekeza mwamuna.

9 Kodi kudzikonda ndi kutani? [2]

A Kuganizira anthu ena

B Kudziganizira iwe mwini

C Kuganizira ana ako

D Kuganizira zodyetsa ana

10 M'nkhani mwawerengayi, liu lofanana ndi 'mbeta'ndi ... [2]

A nkhali.

B cola.

C ucitsizi.

D mbiso.



www.eczpastpapers.com

**Tsopano yankhani mafunso otsatirawa polemba ziganizo zathunthu ndipo zobvomerezeka**

**11** Kodi Mwananiwako anapatsidwa langizo lanji ndi mwamuna wake? [2]

**12** Mwananiwako anaganiza kuti ndi ciani cinali kuondetsa mwana wake? [2]

**13** Kodi Mwananiwako anaululika bwanji kuti anali waumbombo? [2]

**14** Nanga Mwananiwako anacita ciani zitadziwika kuti anali waumbombo? [2]

**15** Dzina lakuli 'Mwananiwako'litanthauza ciani? [2]

## D CIGAWO CACINAI – CINENEDWE [MAMALIKI 30]

**Yankhani mafunso onse asanu am'cigawo ici**

**1** "**Ndi**" ali ndi nchito zina. Lembani ciganizo pa nchito iri yonse ya "ndi" imene yapatsidwa munsimu.

**(i)** Mperekezi ............................................................................ [2]

**(ii)** Mcitiri ............................................................................ [2]

**(iii)** Mlowammalo............................................................................ [2]

www.eczpastpapers.com

**2** **(a)** Kodi alozi ndi ciyani? [2]

**(b)** Lembani ziganizo zoyenera ndi alozi awa.

**(i)** uwo [1]

**(ii)** iyi [1]

**(iii)** ilo [1]

**(iv)** ino [1]

**3** Munsimu muli mau amene apatsidwa. Sonyezani kusiyana kwa mauwa poyagwiritsa nchito mziganizo zoyenera.

**Citsanzo:** Tola/Toola

Tola: Atate atola cola

Toola: Dzulo tinadyera nsima tinyama toola

**(a)** bvika/bviika [2]

**(b)** bvula/bvuula [2]

**(c)** bola/boola [2]



www.eczpastpapers.com

4 **(a)** Kodi maidiofoni ndi ciyani? [2]

**(b)** Lembani ziganizo zoyenera ndi maidiofoni awa.

**(i)** mbee [1]

**(ii)** khuma [1]

**(iii)** gwi [1]

**(iv)** mya mya mya [1]

5 Ziganizo ziri munsimu ndi zolakwika. Tsopano zilembeni molunjika.

**(a)** Ganizani anayenda kusukulu masiku onse. [1]

**(b)** Mpeni wanu ujuwa bwino ndiwo [1]

**(c)** Nyimbo za Likawomba sizimveka mushe [1]

**(d)** Maliyana ayenza bwino galimoto pa mseu [1]

**(e)** Manyumba ya kumudzi kwathu yanapsya [1]

**(f)** Ndaona fulu ndi aphunzitsi pita apa [1]

**Kwatha**

www.eczpastpapers.com



www.eczpastpapers.com